# Nicifukwa Cani Mvuwu Alibe Sisi




Basilio Gimo, David Ker

Carol Liddiment

Sitwe Benson Mkandawire

2

Chichewa ny



Tsiku limodzi, Kalulu analikuyenda mumbali mwamtsinje.



Mvuwu naye analiko kusowera, kuyenda-yenda ndi kudya mauzi.



Mvuwu sanaone kuti kalulu naye alipo ndiponso mosadziwa, anadyaka pakwendo yakalulu. Kalulu anayamba kupunda nakukalipila Mvuwu, “Iwe Mvuwu! suona kuti wanidyaka pakwendo?”



Mvuwu anaphepetsa kwa kalulu “Phepani. Sindinakuoneni. Mundikhulululukile!” Koma kalulu sana mvera phepetso nakalipila Mvuwu “Iwe wacitila dala! Tsiku limodzi uzaona ndizabwezera!”



Kalulu anayenda kusakila moto ndiponso anati “Yenda, kamushoke Mvuwu akacoka mumanzi pakudya mauzu. Anandidyaka!” Moto unayankha, “Palibe bvuto kalulu munzanga. Ndizacita motere”.



Pambuyo pache, Mvuwu analikudya mauzu patali ndi manzi pamene “whoosh!” moto unayamba. Moto unayamba kushoka sisi la Mvuwu.



Mvuwu anayamba kulila nakuthamangila mumanzi. Sisi lake lonse linapya ndi moto. Mvuwu anapitiliza kulira, “Sisi langa lapya ku moto! Sisi langa lonse layenda! Sisi langa labwino!”



Kalulu anakondwela kuwona sisi la Mvuwu lapya. Nipaka lelo, kuyopa moto, Mvuwu samayenda kutali ndi manzi.

# Global Storybooks

globalstorybooks.net

## Nicifukwa Cani Mvuwu Alibe Sisi


Basilio Gimo, David Ker

Carol Liddiment

Sitwe Benson Mkandawire